CHIDZIWITSO

Ngati panopa kapena m'mbuyomo inuyo munagwirapo ntchito mu MGODI WA GOLIDE ku South Africa kuchokera pa 12 March 1965 kufika nthawi ina iliyonse mtsogolo mwake, ndipo munaika moyo wanu pachiswe popuma fumbi la mumgodi motinso mwina munapezekapo ndi matenda a kuwonongeka kwa mapapo chifukwa chopuma fumbili kapena munadwala chifuwa chachikulu ("TB") KAPENANSO ngati munthu amene ankagwira ntchito mumgodi ndiye ankakusamalirani inuyo (mwachitsanzo ngati munali mkazi wake wamtchatho, mwana wake, kapena mkazi wake wongotengana) ndipo pano munthuyo anamwalira, CHONDE WERENGANI CHIDZIWITSO ICHI MWATCHERU CHIFUKWA CHITHA KUKUTHANDIZANI KUDZIWA ZA UFULU UMENE MULI NAWO.

KUMVANA PANKHANI YA CHIPEPESO

Pa May 3, 2018, makampani asanu ndi imodzi awa: African Rainbow Minerals, Anglo American SA, AngloGold Ashanti, Gold Fields, Harmony ndi Sibanye-Stillwater ndiponso makampani ena omwe amagwirira ntchito limodzi, omwe onse pamodzi tikuwatchula kuti ("makampani okhudzidwa ndi nkhaniyi") anamvana kuti apereke chipepeso kwa ogwira ntchito mu migodi ya golide omwe ali oyenera kulandira chipepesochi kapena kwa amene anali kusamaliridwa ndi anthu amene ankagwira ntchito mu migodiyi koma pano anamwalira. Chipepesochi chikuyenera kuperekedwa kwa anthu omwe amagwira ntchito mumakampani okhudziwa ndi nkhaniyi mogwirizana ndi madandaulo omwe gulu la anthu ogwira ntchito kumakampaniwa linakatula ku khoti lalikulu kwambiri la High Court chifukwa cha zinthu zi:

- kuwonongeka kwa thanzi komanso chuma cha ogwira ntchito mumigodi panthawi imene amagwira ntchito mumigodi inayake ku South Africa n'kupezeka kuti adwala matenda a kuwonongeka kwa mapapo kapena matenda a TB, ndi
- kuwonongeka kwa thanzi komanso chuma kwa amene anali kusamaliridwa ndi anthu omwe amagwira ntchito mu migodiyi, omwe anamwalira chifukwa cha matendawa.

Dongosolo lomvana zakuti makampaniwa apereke chipepeso linavomerezedwa ndi khoti lalikulu la High Court ku Johannesburg pa 26 July 2019.

KODI NDANI ALI M'GULU LOLANDIRA NAWO CHIPEPESOCHI?

Pali magulu anayi a anthu omwe ali oyenerera ndipo ngati mukukwanitsa ziyeneretso zonse za gulu limodzi lokha pa anayiwa ndiye kuti ndinu oyenerera m'gulu limenelo. Magulu ake nawa:

Gulu 1:

Aliyense amene:

1. pofika tsiku lomwe chigamulo choperekera chipepeso chiyambe kugwira ntchito wakhala atagwira ntchito yoika moyo wake pachiswe. Mogwirizana ndi zimene anagwirizana pa chigamulochi, tikati "ntchito yoika moyo pachiswe", tikutanthauza ntchito zofotokozedwa mu lamulo lokhudza kudwala chifukwa chogwira ntchito za m'migodi ndi ntchito zina zowopsa (Occupational Diseases in Mines and Works Act, 1973). Zina mwa ntchitozi ndi izi:

(i) ntchito za pansi pa nthaka mkati mwa mgodi wa golide;

(ii) ntchito za kumalo kochapila zovala za anthu ogwira ntchito m'migodi ya pansi pa nthaka;

(iii) ntchito ya kumtaya komwe kumatayidwa zinthu zotsalira akayenga golide;

(iv) ntchito za mu chipinda chomwe amapangiramo kafukufuku kuti adziwe ngati golideyo ali wambambande, komanso kufufuziramo kuti ndi fumbi lochuluka bwanji mum'godimo lomwe anthu amalipuma;

(v) ntchito za komwe amayengerako golideyo, kuphatikizapo kumuphwanya, kumugaya, kumunyamula kumupititsa kwina komanso kumuyenga pomutenthetsa kwambiri kuti asungunuke; komanso

(vi) ntchito za pa mpita pomwe pamadutsa miyala yophwanyidwa pokumba golide poichotsa pansi mu mgodi kupita kunja;

2. aliyense amene patsiku limene chigamulochi chinaperekedwa kapena m'mbuyo mwake, anali atatenga kale matenda owononga mapapo kapena anapuma fumbi la mu mgodi;
3. aliyense amene panopo kapena m'mbuyomo, kuchokera pa 12 March 1965, akugwira kapena ankagwira ntchito yoika moyo pachiswe mu mgodi umodzi kapena migodi ingapo mwa migodi yomwe yatchulidwa pa mndandanda woyamba womwe uli pansi pa chidziwitso chino; komanso
4. aliyense amene sanalandire chipepeso chake panthawi yomwe kampani ya Anglo American South Africa Limited ndi ya AngloGold Ashanti Limited ankapereka chipepeso chomwe anamaliza pa 14 March 2016, ndiponso kampani ya Anglo American South Africa Limited, pa 19 September 2013.

Gulu 2:

Aliyense amene anali kusamalidwa ndi munthu yemwe panopa, padeti limene chigamulochi chinaperekedwa anali atamwalira koma ali mu Gulu 1 lili pamwambali.

Gulu 3:

Aliyense amene:

1. kuchoka pa tsiku lomwe chigamulochi chinaperekedwa anagwirapo ntchito yoika moyo pachiswe;
2. pofika kapena lisanafike tsiku lachigamulochi anali atam'peza ndi chifuwa chachikulu cha TB; komanso
3. omwe panopo akugwira kapena omwe m'mbuyomo anagwirapo ntchito yoika moyo pachiswe, patadutsa pa 12 March 1965, mu mgodi umodzi kapena migodi ingapo mwa migodi yomwe yatchulidwa kumapeto kwa chidziwitso chino.

Gulu 4:

Aliyense amene anali kusamalidwa ndi munthu yemwe panopa, padeti limene chigamulochi chinaperekedwa anali atamwalira koma ali mu Gulu 3 lili pamwambali.

KODI MFUNDO ZIMENE ANAMVANA PA CHIPEPESOCHI ZIYAMBA LITI KUGWIRA NTCHITO?

Mfundozi sizinayambe kugwira ntchito chifukwa mbali zina zomwe anagwirizana pa chigamulo chija sanazikwaniritse. Mbali zimenezi zikakwaniritsidwa, makampani okumba golidi okhudzidwa ndi nkhaniyi adzakhazikitsa thumba, lotchedwa TSHIAMISO TRUST.

Chipepesochi chikadzayamba kuperekedwa:

- Makampani okumba golidi okhudzidwa ndi nkhaniyi adzasonkherana ndalama zimene anagwirizana n'kuziika mu thumba la Tshiamiso Trust ndipo kenaka adzayamba kulipira anthu oyenera kulandira chipepesowo.
- Anthu onse okhudzidwa, **kupatulapo omwe anasankha kuti asawerengedwe m'gululi, adzakhala omasuka kuitanitsa ndalama zachipepeso chawo ku Tshiamiso Trust**.
- Dongosolo la mmene mungaitanitsire ndalama ku Tshiamiso Trust lidzaikidwanso mumalo ofalitsira mauthenga komanso pa webusayiti iyi: www.silicosissettlement.co.za.
- Tshiamiso Trust idzapereka ndalama zachipepeso kwa onse oitanitsa ndalamazi **amene ali oyenerera**. Munthu woyenerera kuitanitsa chipepeso ndi aliyense amene ali m'magulu anayi aja amene akukwaniritsa ziyeneretso za Tshiamiso Trust.
- Anthu onse okhudzidwa akuyenera kulemba zonse zofunika mufomu yoitanitsira ndalama zachipepesozi n'kuitumiza ku Tshiamiso Trust ndipo angafunikenso kupimidwa kuchipatala pofuna kutsimikizira kuti akuyenereradi chipepesochi.

Chipepesochi chikadzayamba kuperekedwa, anthu oyenerera adzalandira ndalamazo kamodzi ndipo kuchuluka kwa ndalama zake ndi pakati pa R10 000 ndi R250 000, malingana ndi matenda amene munthuyo akudwala ndi mmene matendawo akulira. Ngati patakhala zifukwa zina zomveka, mwina zingatheke kuwonjezera ndalamazi mpaka kufika R500 000.

Ndondomeko yonse ya chipepesochi ndiponso chigamulo cha ku khoti pankhaniyi zikupezeka pa www.silicosissettlement.co.za kapena mungazipeze kwa maloya oyendetsa nkhaniyi **(onani mmene mungawapezere pamunsipa)**.

SIPOFUNIKA KULIPIRA MUNTHU WINA ALIYENSE KUTI AKUTHANDIZENI KUITANITSA NDALAMA ZANU ZA CHIPEPESO

KODI NDIKUYENERA KUTANI KUTI NDIKHALEBE PA MNDANDANDA WA ANTHU OYENERA CHIPEPESO?

NGATI MULI M'GULU LOVOMEREZA CHIPEPESO NDIPO MUKUFUNA KUDZALANDIRA NAWO, SIMUYENERA KUCHITA CHILICHONSE PAKALI PANOPO.

Inde, simufunikira kuchita chilichonse kuti mulandire nawo chithandizochi, komabe ngati mungafune kusonyeza chidwi chanu pankhaniyi mwakutumiziratu dzina lanu ndiponso zonse zokhudza mmene munthu angakupezereni, teroni polemba zofunika pa fomu kapena polembetsa za chidwi chanuchi pa webusaiti ya www.silicosissettlement.co.za.

NGATI SIMUKUFUNA KUKHALA M'GULULI

NGATI MULI M'GULU LOVOMEREZA ZIMENE ANAMVANA PA CHIPEPESOCHI, NDIYE KUTI MULI KALE PA MNDANDANDA WOLANDIRA CHIPEPESO POKHAPOKHA NGATI NOKHA SIMUKUFUNA N'KUTSATA NDONDOMEKO YOTULUKIRA M'GULULI. Ngati simukufuna kukhala m'gulu lovomereza chipepeso chija, kapena ngati mukufuna kukhala ndi ufulu wokadandaula nokha ku khoti, tsatirani ndondomeko yotsatirayi kuti musakhale nawo m'gululi.

Kuti mutuluke m'gululi, mukuyenera **KULEMBA ZOFUNIKA NDIPONSO KUSAINIRA FOMU (YOYENERERA KWA INUYO), KAYA NDI FOMU A, KAYA NDI FOMU B; KAYA NDI FOMU C; KAPENA KAYA NDI FOMU D NDIPO ITUMIZENI PAMODZI NDI ZIKALATA ZINA ZONSE ZOFUNIKIRA, KWA MKULU WOYANG'ANIRA NTCHITOYI SNG Grant Thornton** pasanafike pa 24 November 2019.

Fomuyi ikuyenera kusainidwa ndi munthu wovomerezedwa mwalamulo (commissioner of oaths). Pa siteshoni ya polisi iliyonse ku South Africa pamakhala wapolisi wina wovomerezedwa mwa lamulo kusainira.

KUTI MUTULUKE M'GULULI, KAPEREKENI FOMU YANU IJA KOMANSO ZIKALATA ZONSE ZOYENERERA, PAMANJA KAPENA PA FAX KAPENANSO PA EMAIL POGWIRITSIRA NTCHITO ZOTSATIRAZI: SNG Grant Thornton

Adiresi ya kalata yapamanja: 20 Morris Street East, Woodmead, Johannesburg 2191

Nambala ya Fax: +27 11 234 0933

Adiresi ya email: silicosissettlement@sng.gt.com

Simungatuluke m'gululi pongoimba foni komabe mungathe kuimba manambala ali m'munsiwa kuti mudziwe zambiri za mmene mungatulukire.

Aliyense m'gululi amene akufuna kutulukamo ayenera kulemba zofunika ndi kusainira fomu ina yapadera.

Mukapereka fomu yofotokoza kuti mukufuna kutuluka m'gulu, Mkulu Woyang'anira Ntchitoyi angathe kulumikizana nanu kuti amvetse zina ndi zina.

MUNGATHE KUPEZA MAFOMUWA PA www.silicosissettlement.co.za **KAPENA KWA MALOYA A M'GULULI. MALOYA ANGATHENSO KUKULANGIZANI NJIRA YOSAVUTA YOPEZERA MAFOMUWA (ONANI PAMUNSIPA ZA MMENE MUNGALUMIKIZIRANE NAWO).**

* ONETSETSANI KUTI MWASAINA FOMU YOLONDOLA YOTULUKIRA M'GULU. NGATI MUKUFUNA THANDIZO PA MBALI IMENEYI, GWIRITSIRANI NTCHITO ZIMENE TALEMBA PAMUNSIPA.

KUTI MUDZIWE ZAMBIRI ZA KUITANITSA NDALAMA ZA CHIPEPESO, CHIGAMULO CHOKHUDZA NKHANIYI NDIPONSO KUTULUKA M'GULU:

- Tsegulani www.silicosissettlement.co.za;
- Imbani nambala yoimba ulere ya pa Malo Oyankha Mafoni pa nambala iyi 0801 000 240 or 0800 110 110. Malo oyankha Mafoni okhudza nkhaniyi adzakuthandizani mwaulere, ndipo foni yake ndi yaulere ngati mukuimbira m'dziko la South Africa;
- Tumizani uthenga woti "Chonde ndiimbireni" ku nambala iyi 072 557 8077 or 079 835 7179.

Mungathenso kupeza maloya amenewa pa mafoni ndi ma adiresi otsatirawa:

Richard Spoor Incorporated Attorneys	Abrahams Kiewitz Incorporated	Legal Resources Centre
Foni: +27 (0)11 482 6081; Fax: +27 (0)11 482 1419 info@rsinc.co.za; P.O. Box 303 Parklands, 2121 Adiresi ya komwe akupezeka: Eton Building, Sherborne Square 5 Sherborne Road Parktown, Johannesburg	Foni: +27 (0)21 914 4842 Fax: +27 (0)21 914 1455 classaction@ak.law.za; P.O. Box 3048, Tygervalley, 7536, Cape Town Penthouse, 6th Floor, Imperial Terraces, Carl Cronje Drive, Tyger Waterfront, Tygervalley, Cape Town	Foni: +27 (0)11 836 9831 Fax: +27 (0)11 834 4273 silicosisclass@lrc.org.za P.O. Box 9495, Johannesburg, 2000 Bram Fischer Towers, 16th Floor, 20 Albert Street, Marshalltown, Johannesburg

Annexure A: Participating mines

SA Land
Daggafontein
East Daggafontein
Elandsrand
Deelkraal (also called Elandskraal)
Kusasalethu
Western Holdings (1,2,3,4,6,7) (ARMGold)
Matjhabeng (Western Holdings other 4 shafts
Kudu, Nyala, Sable, Eland which were former Freddies and Free State Geduld shafts)
Saaiplaas 2,3
Saaiplaas 4,5 (Masimong) (FreeGold 3)
Free State Geduld
Free State Cons
FreeGold 2 and 4
Freddies 7 and 9 (to Kades Barnea cc, Pamodzi, Target mine)
Freegold 2, 4 (Tshepong, Phakisa)
President Brand
President Steyn
Steyn 1,2 (to Kades Barnea, Pamodzi, Bambanani)
Steyn 3,4 (FreeGold 1, then Bambanani)
Brand 1, 2, 3, 5 (Steyn 5 to 8)
HJ Joel / Joel
Western Reefs (merged with Vaal Reefs)
Vaal Reefs (1,3,4,5,6,7)
Vaal Reefs 2
Vaal Reefs 8 (Great Noligwa)
Vaal Reefs 9 (Kopanang)
Vaal Reefs 10 (Tau Lekoa)
Vaal Reefs 11 (Moab Khotsong)
Western Deep Levels
Mponeng (South Mine WDL 1)
Tau Tona (East Mine WDL 3)
Savuka (West Mine WDL 2)
St Helena
Evander (incl Kinross, Leslie, Bracken and Winkelhaak mines)
Randfontein Estates
Doornkop
Cooke 1, 2 and 3 (Rand Uranium)
Cooke 4 (Ezulwini)
Unisel
Harmony mine
Merriespruit
Hartebeesfontein
Loraine (Shafts 1,2 and 3)
Zandpan
Virginia mine
Village Main Reef
Western Areas (to South Deep)
South Deep
Beatrix (including Oryx)
Oryx (to Beatrix)
Driefontein (including East Driefontein, West Driefontein and Driefontein Cons)
Kloof (including Leeudoorn from 1 Jan 1993, Libanon and Venterspos)
St Helena (Beisa section)